KODI
KUWUKIRA KWA MSIPU MU AFRICA
NDI KOTANI?



duduceelho.com

Kuwukira kobiriwira kutanthauza kupanga mbeu za mtundu wobereka kwambiri zomwe zimachedwanso mbeu zopititsidwa pa tsogolo kapenanso mbeu zopatsidwa chikalata cha chibvomelezo. Mbeu zimenezi zipangidwa ndi cholinga chochulukitsa muyeso wa zokolola pa yekala imodzi ngati mbali ya njira zamakono zomwe zimagwiritsa nchito fataleza wa mankhwala, mankhwala a mbeu, nkhani ya za chuma, kuthandiza kupeza misika ya zokolola ndi zina zotere.

Anthu womwe akhalila kumbuyo kuwukira kobiriwira amati njira za kuwukira kumeneku zimapititsa patsogolo kuchilikitsa kwa ulimi, unyinji wa chakudya ndi kupititsa patsogolo kadyedwe. Ganizo lawo ndi lakuti alimi azagula zofunikira mu ulimi zomwe zizagulitsidwa pa mtengo wotsika kwa zaka zing'ono poyamba ulimi umeneu. Ichi akuti chizapangitsa kuti akhale ndi zokolola zambiri zomwe zizagulitsidwa pa ndalama zambiri. Pambuyo pake azakhala ndi ndalama zambiri zakuti chakudya chokwana chakuti adye chaka cha mawa ndi kugula zofunika pa ulimi wa zaka zakutsogolo.

Koma mu umoyo sizimakhala choncho ndipo ndi alimi wochepekela omwe angaphindule ku njira imeneyi.

www.acbio.org.za info@acbio.org.za Tel +27 (0)11 486 1156

african centre for biodiversity